EXAMINATION NO.: ____________________

# THE MALAWI NATIONAL EXAMINATIONS BOARD

## 2026 JUNIOR CERTIFICATE EXAMINATION

# CHICHEWA

Subject Number: J032/I

Friday, 5 June

Time Allowed: 1 h 30 min
11:00 am – 12:30 pm

## PEPALA LOYAMBA

(Malikisi 50)

**Malangizo**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi awiri.**

2. Lembani **nambala yanu ya mayeso** pamwamba pa tsamba **lililonse** la pepalali.

3. Yankhani mafunso **onse** m'gawo **A** ndi m'gawo **C**. M'gawo **B**, yankhani funso **limodzi** lokha.

4. Muchitebulo chili pambalichi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha kuyambira funso **21 mpaka 23** pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.

5. Perekani pepalali kwa oyang'anira mayeso nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1-5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21 | | | |
| 22 | | | |
| 23 | | | |
| | | | |
| | Total | | |



©2026 MANEB

Onani paseri/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## Gawo A (Malikisi 20)

**Langizo:** Zungulizani lembo lokhoza (**A**, **B**, **C** kapena **D**) m'mafunso otsatirawa.

**Mafunso 1 mpaka 5:** Sankhani mitundu ya mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**1.** Zuze, mlesi sagwira nawo ntchitoyi.
- A. lamwinimwini
- B. lapadera
- C. lachinthu chokhudzika
- D. launyinji

**2.** Khwimbi la anthu lapita kumeneko.
- A. lopanda mwinimwini
- B. lachinthu chosakhudzika
- C. lamwinimwini
- D. launyinji

**3.** Mpingo wathu umagawa zinthu kwa osowa.
- A. launyinji
- B. lamwinimwini
- C. lopanda mwinimwini
- D. lachinthu chosakhudzika

**4.** Mzimu umenewu sungatukule dziko.
- A. lamwinimwini
- B. lachinthu chosakhudzika
- C. lapadera
- D. lachinthu chokhudzika

**5.** Shire ndi mtsinje waukulu.
- A. lopanda mwinimwini
- B. lachinthu chosakhudzika
- C. launyinji
- D. lamwinimwini

**Mafunso 6 mpaka 10:** Sankhani ziganizo zomwe zalembedwa molondola.

**6.**
- A. Muzipita kwanu
- B. Mudzipita kwanu.
- C. Muzipita kwanu.
- D. Mudzipita kwanu

**7.**
- A. Phili la Zomba ndi lokongola zedi.
- B. Phili la Zomba ndi lokongola zedi
- C. Phiri la Zomba ndi lokongola zedi.
- D. Phiri la Zomba ndi rokongola zedi.

**8.**
- A. Lero ndikutsala kudya.
- B. Lero ndikusala kudya.
- C. Lelo ndikusala kudya
- D. Lelo ndikutsala kudya

**9.**
- A. Iye akusasa njinga yake kuti ndigule.
- B. Iye akusatsa njinga yake kuti ndigule.
- C. Iye akutsasa njinga yake kuti ndigule.
- D. Iye akutsatsa njinga yake kuti ndigule.

**10.**
- A. Tsoka sasimba koma mwayi.
- B. Soka sasimba koma mwayi.
- C. Tsoka satsimba koma mwayi.
- D. Tsoka tsatsimba koma mwayi.

Mafunso akupitirira/...

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Mafunso 11 mpaka 15:** Sankhani mikuluwiko yofanana m'matanthauzo ndi yomwe ili m'munsiyi.

**11.** Tsabola wakale sawawa.
- A. Mawu aakulu akoma akagonera.
- B. Bza sapita kawiri.
- C. Ukayendera mzengo usamati asakhwi afumbula.
- D. Njuchi zikachuluka siziika.

**12.** Mwana wang'ona sakulira dziwe limodzi.
- A. Likawomba wotheratu.
- B. Mwala wogudubuzika suyanga ndere.
- C. Lero lomwe lidadetsa nthengu.
- D. Ziliko n'kulinga utatosako.

**13.** Chibwereza chidaphetsa kunda.
- A. Padakafunda padajiwitsa galu.
- B. Tsabola wakale sawawa.
- C. Ali dere n'kulinga utayenda naye.
- D. Mphini yobwereza ndi yomwe imawala.

**14.** Padakafunda padajiwitsa galu.
- A. Safunsa adadya phula.
- B. Kali kokha n'kanyama tili tiwiri n'tianthu.
- C. Ndikuona adalasa yabere.
- D. Kuona maso a nkhono n'kudekha.

**15.** Kanthu n'kako uvundukula nupenya.
- A. Ali dere n'kulinga utayenda naye.
- B. Zathu salowa m'khola.
- C. Kugona pakati n'kuyambirira.
- D. Ichi chakoma icho chakoma pusi adagwa chagada.

**Mafunso 16 mpaka 20:** Sankhani ntchito ya mphatikiri yemwe watsekedwa mzere kunsi kwake m'ziganizo zotsatirazi:

**16.** Kanjinga kameneko sindingakwerenso.
- A. kusonyeza kubwereza
- B. kuthandizira kulemekeza
- C. kusonyeza kunyoza
- D. kusonyeza kukayika

**17.** Ikani ndiwozo mumphika.
- A. kusonyeza malo
- B. kuthandizira kupanga dzina
- C. kusonyenza nthawi
- D. kusonyeza yemwe wachita ntchito

**18.** Dzukani pogonapo.
- A. kusonyeza nthawi
- B. kusonyeza malo
- C. kusonyea kulemekeza
- D. kusonyeza kulamula

**19.** Sudya nawo nsimayi lero.
- A. kusonyeza nthawi
- B. kusonyeza kutsutsa
- C. kusonyeza kulamula
- D. kusonyeza yemwe wachita ntchito

**20.** Chikabudula ichi ndi chokongola zedi.
- A. kusonyeza kulemekeza
- B. kusonyeza kunyoza
- C. kusonyeza kuchepetsa
- D. kusonyeza kukulitsa

Mafunso akupitirira/...

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Gawo B** (Malikisi 20)

**Malangizo:**

**(i)** Yankhani funso **limodzi** lokha m'gawoli.

**(ii)** Lembani **Chimangirizo** kapena **Kalata** pa masamba **5 ndi 6**. Mawu a chimangirizo kapena kalata asachepere **150** koma asapitirire **200**. Malikisi adzaperekedwa pakayalidwe ka chimangirizo kapena kalata, malamulo a chiyankhulo, mfundo ndi kagwiritsidwe ntchito koyenera ka nsinjiro za chiyankhulo.

**21.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu:

Ubwino wosamalira nyama zam'nkhalango

**(Malikisi 20)**

## KAPENA

**22.** Lembani kalata kwa mnzanu yomufotokozera kufunika kwa ntchito za chitukuko m'dera lanu.

**(Malikisi 20)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Mafunso akupitirira/...

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Gawo C** (Malikisi 10)

**Langizo:** Yankhani magawo onse a funso ili.

23. a. Werengani malonje ali m'munsimu ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

"Zikomo nonse chifukwa chobwera mwaunyinji kudzamanga nyumba yoti ophunzira athu azigonamo. Ndithokoze kuti pa ntchitoyi panalibe gwala."

(i) Kodi malonjewa akuchitikira kuti?

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(ii) Angayankhule malonjewa ndani?

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(iii) Perekani mfundo **imodzi** yosonyeza kuti anthu akuyankhulidwa m'malonjewa ndi ogwirizana.

_______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(iv) Kodi mawu woti "gwala" akutanthauzanji?

_______________________________________________

**(Malikisi 2)**

b. Perekani malangizo **atatu** omwe mungapereke kwa wophunzira mnzanu kuti apewe kudwaladwala.

(i) _______________________________________ **(Malikisi 1)**

(ii) _______________________________________ **(Malikisi 1)**

(iii) _______________________________________ **(Malikisi 1)**

c. Tchulani njira **ziwiri** zofalitsira mauthenga a chionetsero cha zaulimi kumudzi.

(i) _______________________________________________

**(Malikisi 1)**

(ii) _______________________________________________

**(Malikisi 1)**

# MAFUNSO ATHERA PANO

**NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa asanu ndi awiri.**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

BLANK PAGE

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com